PHUNZIRO LA 9

1. Kodi Mulungu anamaliza kulenga dziko la pasi ndi kwamba?
-Inde.

2. Kodi Mulungu amati akayiyamba ntchito, amayisiya osayimaliza?
-Iyayi.

3. Kodi chifukwa chiyani Mulungu amati akayiyamba ntchito, sayisiya osayimaliza?
-Chifukwa chakuti palibe china chilichose chimene chingamuletse Mulungu kumaliza ntchito yake.

4. Kodi Mulungu akayiyamba ntchito, anthu angathe kuyiletsa ntchito Yakeyo?
-Iyayi.

5. Kodi Mulungu akayiyamba ntchito, Satana angathe kuyiletsa ntchito Yakeyo?
-Iyayi.

6. Kodi Mulungu akayiyamba ntchito, ziwanda zingathe kuyiletsa ntchito yakeyo?
-Iyayi.

7. Kodi Mulungu akalonjeza kuti achita chinthu china chake, amachichita chinthucho?
-Inde.

8. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapuma pa tsiku la chisano ndi aŵiri?
-Chifukwa chakuti anamaliza kulenga zinthu zonse zimene anaganiza kuti azilenge.

9. Kodi pachiyambi Mulungu amkatumiza mvura kudzatsilira pa dziko la pasi?
-Iyayi.

10. Kodi pachiyambi Mulungu amkatsilira bwanji pa diko la pasi?
-Dziko la pasi limkatsililidwa ndi madzi amene amkatuluka kuchokera pasi pa nthaka.

11. Kodi Mulungu anamutsagulilira ndani munda wa Edeni?
-Adamu.

12. Kodi Mulungu anamupempha Adamu kuti akamuyike m'munda wa Edeni?
-Iyayi.

13. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanamupemphe Adamu kuti akamuyike m'munda mwa Edeni?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu, Adamu ndi wa Mulungu.

14. Kodi anthu onse ndi zinthu zonse ndi za ndani?
-Mulungu.

15. Kodi dzina la Mtengo Woyamba umene Mulungu anadzala pakati pa munda wa Edeni linali chiyani?
-Mtengo Wopereka Moyo.

16. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anadzala Mtengo Wopereka Moyo pakati pa munda wa Edeni?
-Mulungu amkafuna kuti Adamu adye zipatso zochokera mu Mtengowo kuti akhale ndi moyo mpaka kalekale.

17. Kodi dzina la mtengo, chipatso chimene Mulungu anamulamula Adamu kuti asadye linali chiyani?
-Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

18. Kodi Adamu anakadya chipatso cha mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa, chinakamuchitikira chiyani?
-Adamu anakafa.

19. Kodi imfa ndi chiyani?
-Imfa ndi kusiyana ndi Mulungu, wopereka moyo.
-Imfa ndi kusiyana kwa thupi ndi moyo.
-Imfa ndi kusiyana kupita ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Tiyeni tiŵerenge zimene analamkhula Mulungu, Iye atamulenga Adamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:18

18-Ambuye anati, "Sibwino kuti munthuyu akhale yekha. Ndipanga mzake wakuti adzimuthandiza."

-Mulungu anaganiza zakuti Adamu asakhale yekha.
-Mulungu yekha anaganiza zomupangira mkazi Adamu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaganiza zomupangira mkazi Adamu?

-Chifukwa chakuti Mulungu anamukonda Adamu kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mulungu samkafuna kuti Adamu akhale yekha.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:19-20a

19-Ambuye Mulungu anatenga dothi ndi kuwumba nyama ndi mbalame zonse. Ndipo anabwera nazo kwa munthu uja kuti azipatse mayina. Mwakuti mayina amene Adamu anazitcha, mayina ake ndi omwewo.
20-Chomcho munthu uja anapereka mayina kwa nyama, mbalame zonse ndi za moyo zonse za ku thengo.

-Pachiyambi, Mulungu anamupanga Adamu kukhala oyang'anira  dziko lonse la pasi.

-Pachiyambi, Mulungu anamupanga adamu kukhala oyang'anira nyama zonse.

-Mulungu anamuwuza Adamu kuti apereke mayina kwa nyama zonse.
-Chomcho Adamu anapereka mayina kwa nyama zonse.

-Komabe pa nthaŵi yimeneyi Adamu anali yekha pa dziko la pasi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:20b

20-Komabe Adamu analibe mzake wakuti adzimuthandiza.

-Kodi Mulungu analenga anthu ndi nyama mofanana?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu analenga anthu mosiyana bwanji ndi nyama?

-Mulungu sanalenge nyama mu chifanizo Chake.
-Mulungu anaŵalenga anthu okha mu chifanizo Chake.

-Anthu angamudziŵe Mulungu koma nyama sizingamudziŵe Mulungu.
-Anthu angamukonde Mulungu koma nyama sizingamukonde Mulungu.
-Anthu angamumvere Mulungu koma nyama sizingamumvere Mulungu.

-Kodi Adamu akasangalala, bwezi akumalankhulana ndi ndani?

-Palibe.

-Kodi Adamu akakhala ndi funso, bwenzi akumalankhulana ndi nyama?
-Iyayi.

-Kodi nyama bwezi zili mzake woyenera wa Adamu?
-Iyayi.

-Adamu amkafuna mzake wakuti azilankhulana naye.

-Chifukwa chakuti Mulungu anamukonda Adamu, Mulunguyo anaganiza zomupangira Adamu mkazi.

-Kodi Adamu anakatha kuzipangira mkazi wa iye yekha?
-Iyayi.

-Kodi Satana ndi ziwanda zake anakatha kumupangira Adamu mkazi?
-Iyayi.

-Kodi ndani yekha amene anakatha kumupangira mkazi Adamu?
-Mulungu.

-Tsiku lina, Mulungu anamupangira mkazi Adamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:21-22

21-Chomcho Ambuye Mulungu anamugoneka tulo lalikulu munthu uja, ali chigonele chomchija, Mulungu anachotsa nthiti imodzi ya munthuyo, ndipo anatseka ndi mnofu pamene anachotsapo.
22-Kenako Ambuye Mulungu anamupanga munthu wamkazi kuchokera ku nthiti imene anayichotsa kwa mamu-

na uja, ndipo Mulungu anabwera naye mkaziyo kwa mamunayo.

-Mulungu yekha ndi amene anatha kupanga mkazi wa Adamu.

-Mphamvu ya Mulungu siyitha.
-Palibe chimene Mulungu angalephere kuchichita.

-Mulungu anapanga munthu wamkazi oyamba, ndikumupereka kwa Adamu ngati mphatso.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi munthu wina atakupatsani inu mphatso yayikulu, mungamayisamalire bwino?
-Inde.

-Kodi munthu wina atakupatsani inu ng'ombe , mungamayisamalire bwino?
-Inde.

-Kodi munthu wina atakupatsani inu galimoto, mungamayisamalire bwino?
-Inde.

-Mulungu anapanga munthu wamkazi oyamaba, ndipo anamupereka kwa Adamu ngati mphatso.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu adzimusamalira mkazi wake.
-Mulungu amkafuna kuti Adamu adzimukonda mkazi wake kwambiri.

-Tiyeni tiŵerenge zimene Adamu ananena pamene Mulungu anamupatsa iye mkazi:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:23-24

23-Munthu uja anati, “Uyu tsopano ndi fupa lochokera ku mafupa anga ndipo mnofu wochokera ku mnofu wanga; ndipo adzatchedwa kuti,“mkazi” chifukwa anachokera mwa mamuna.

24-Pachifukwa ichi, mamuna adzasiya bambo ake ndi mayi ake ndi kudziphatika yekha kwa mkazi wake, ndipo adzakhala thupi limodzi.

-Mulungu anamupangira mamuna, mkazi kuti adzikwatirana.
-Mulungu anamupangira mamuna, mkazi kuti adzikhalira limodzi.
-Mulungu anamupangira mamuna, mkazi kuti adzibereka ana.

-Zonse zimene amachita Mulungu ndi zabwino zokhazokha.
-Zonse zimene amachita Mulungu ndi zabwino kwambiri.
-Zonsezo ndi chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.

-Mulungu saganiza zoyipa.
-Mulungu salankhula zoyipa.
-Mulungu sachita zoyipa.

-Kodi mukuganiza kuti Adamu anali osangalala palandira mphoto yayikulu ya mkazi?
-Inde.
-Adamu anali osangalala kwambiri.

-Kodi dzina la mkazi wa Adamu linali ndani?
-Dzina la mkazi wa Adamu linali Hava.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:25

25-Mamuna ndi mkazi wake uja, onse anali maliseche, koma samkachita manyazi.

-Pachiyambi, Adamu samkachita manyazi.
-Pachiyambi, nayeso Hava samkachita manyazi.

-Pachiyambi, Mulungu analenga Adamu ndi Hava ali anthu abwino kwambiri.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava samkadziwa tchimo lina lili-lonse.

-Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkayenda ndi Mulungu ndipo amkasangalala kwambiri.